# CARMUSHKA PRIMARY SCHOOL

2021 STANDARD 8 END OF TERM 1 EXAMINATIONS

## CHICHEWA

(100 Malikisi)

Lachinayi,29 Epulo.

Nthawi :2hrs 15mins
10:00m’mawa-12:15masana

Dzina : ______________________________________________________________________________

## Malangizo

1. **Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba asanu ndi limodzi.**
2. Pepala ili lili ndi magawo anayi; Gawo A, B, C ndi D.
3. Lembani dzina lanu pamwamba pa tsamba lililonse.
4. Lembani chimangirizo kapena kalata mu Gawo A ndipo muyankhe mafunso onse mu Gawo B, C ndi D
5. Lembani yankho la mu Gawo A pa pepala lomwe mwapatsidwa
6. Yankhani mafunso a mu Gawo D pozunguliza lembo lokhonza pa funso lililonse.
7. Muchitebulo chili pamwambachi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.
8. Perekani kwa oyanganira kulemba mayeso (invigilator) pepala lonseli nthawi ikakwana.

| Nambala ya funso | Chongani ngati mwayankha | Musalembe Muno |
|---|---|---|
| 1 | | |
| 2 | | |
| 3 | | |
| 4 | | |
| 5-44 | | |
| | | |

*G-Tech*

## GAWO A: MALIKISI 30

**Langizo;Yakhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali mmunsiwa. Sakhani mutu wa chimangirizo kapena wa kalata.Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere 100 koma asabzole 150.**

**1.** Lembani chimangirizo pa mutu uwu; **TSIKU LOSAYIWALIKA.**Mwazina tsatani izi polemba:

**Ndime yoyamba**

- Lidali tsiku liti?
- Komwe mudali pa tsikulo.

**Ndime yachiwiri**

- Zomwe zidachitika pa tsikulo.
- Momwe mudakhudzidwira ndi zochitikazo.
- Zomwe zidachititsa tsikulo kukhala lotsayiwalika

**Ndime yachitatu**

- Mudaphunzirapo chiyani pa tsikulo.

**KAPENA**

**2. Lembani kalata kwa makolo anu yopempha ndalama zolipilira ulendo womwe sukulu yanu yakonza wokawona nyama kunkhalango ya boma. Mwazina tsatani izi polemba**:

**Ndime yoyamba**

- Dzina la khalango komwe mudzapite.
- Tsiku la ulendo
- Ndalama za ulendo

**Ndime yachiwiri**

- Zomwe mukuyembekezera kukaona.
- Kufunika kwa ulendo p amaphunziro anu.

**Ndime yachitatu**

- Chitsangalalo chomwe mudzakhale nacho mukazapita nawo ku ulendowo.

## GAWO B: KUMVETSA KHANI (MALIKISI 20)

**3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenako yakhani mafunso otsatirawa**

**ANA A SUKULU**

Anyamata ndi atsikana amapita ku sukulu kukaphunzira zinthu zambiri monga; ukhondo, khalidwe la bwonindikutsatilamalamulo.Ukhondo amaphunzira kuti adzilewa matenda ndikukhala ndi moyo wathanzi.Uve umadzetsa tizilombo toyambitsa matenda omwe munthu atha kufa nawo.Ana amaphunziranso zamakhalidwe abwino .Izi zimawathandiza kulemekeza makolo awo ndi anthu ena akulu.Kusukulu ana amaphunzira mosiyanasiyana. Ana ena amalimbikira sukulu koma ena amachita ulesi. Ana aulesi kawirikawiri amalephera mayeso pomwe olimbikila komanso achangu amakhonza mayeso.

Chinthu chomwe mwana wa sukulu wina aliyense ayenera kudziwa ndi chakuti kusukulu kulibe kapolo kapena mfulu, kawirikawiri kusukulu kumapezeka anyamata ena komanso atsikana ena omwe amavutitsa anzawo achilendo, kusukulu kumene kuli aphunzitsi odziwa udindo wawo, ana onzunza anzawowa amalangidwa. Koma kukoma mtima ndi chinthu chofunika kwambiri popeza kumaonetsa kutsiyana pakati pa anthu ndi nyama.

Mwana wa sukulu sayenera kukwatiwa kapena kukwatila. Ili ndi limodzi mwamalamulo apa sukulu. Malamulo amatchinjiriza ophunzira ngakhale ophunzirao amaganiza kuti malamulo amachepetsa ufulu wawo. Aphunzitsi ayenera kufotokodzera ophunzirawo ubwino wotsatila malamulo popewa kuti patsogolo angadzanong'oneze bondo.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizère ilipansi pa funso lililonse.**

I. Perekani zinthu ziwiri zomwe anyamata ndi atsikana amakaphunzira kusukulu.

________________________________________ (malikisi 1)

________________________________________ (malikisi 1)

II. Kodi ukhondo ndi wofunika bwanji kwa ophunzira?

________________________________________(1 malikisi)

III. Tizilombo toyambitsa matenda timabwera bwanji ?.

________________________________________ (1 malikisi)

IV. N'chifukwa chiyani ana ena amalephera mayeso ?
____________________________________________________________ (1 malikisi)

V. Lembani khalidwe loipa lomwe ophunzira ena amakhala nalo kusukulu (2 malikisi)
____________________________________________________________

VI. Perekani mawu ofanana m'matanthauzo ndi awa:
- Uve ________________________________________________(1 malikisi)
- achilendo ____________________________________________(1 malikisi)
- kutchinjiriza ___________________________________________ (1 malikisi)

VII. Ndi aphunzitsi otani amapereka chilango kwa ana akhalidwe loipa ?
_______________________________________________________ (2malikisi)

VIII. Kodi kukoma mtima n'kofunika bwanji?
_______________________________________________________ (2 malikitsi)

IX. .Perekani tanthauzo la chining'aichi "angadzanong'onezebondo"
_________________________________________________________ (2 malikisi)

X. Lembani udindo uwiri wa aphunzitsi
____________________________________________________________ (1 malikisi)
____________________________________________________________ (1malikisi)

XI. N'chifukwa chiyani, ophunzira amadana ndi malamulo a pasukulu?
__________________________________________________________ (1 maliksi)

## GAWO C : MALIKISI 10

**Yankhani mafunso onse awiri m'gawoli**

**4. a.Werengani kankhanika ndipo muyakhe mafunso otsatilawa.**

A Banda: Odi!!..Odi!!..
ANambewe: Eee tikuopeni, Bambo?
ABanda: Musandiope kwenikweni ,kodi amuna anu alipo?
ANambewe: Ayi ,palibe .momwe achokera m'mawa.
ABanda: chabwino sindivutika popeza inu mulipo. Mawa kuli liwamba. Nachi chimanga chofiira mudzawapatse amuna anu.

**MAFUNSO**

(i).Kodi ndi uthenga wanji omwe a Banda abweretsa n'kulonjera kwawo ndi a Nambewe?
____________________________________________________________ (1malikisi)

(ii).kodi m'malonjewa,a Banda ndi ndani ?
____________________________________________________________ (1malikisi)

(iii)Nanga chimanga chofiira chitanthauzanji m"malonje?
__________________________________________________________ (1 malikisi)

(iv)Tchulani chinthu chimodzi chofunika pa msika pofuna kupititsa ukhondo patsogolo.
___________________________________________________________ (1malikisi)

(v)Perekani kufunika koyezetsa magazi mwamuna ndi mkazi asanakwatilane.
___________________________________________________________ (1 malikisi)

**Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:**

i. mphulu ______________________________________________________________
ii. kama _______________________________________________________________
iii. mbee _______________________________________________________________
iv. chigalagaza ___________________________________________________________

v. dovu ____________________________________________

## GAWO D: (MALIKISI 40)

**Zungulitsani lembo (A, B,C kapena D) m'mafunso otsatirawa.**

**Mafunso 5 mpaka 9: Sakhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi**

5. Mwana wanga wadwala **kwambiri**
   A. Muonjezi C. mperekezi
   B. mfotokozi D.mlowammalo
6. Malaya **akudawo** ndi ake
   A. Mperekezi C.Mlowammalo
   B. Mneni D.Mfotokozi
7. **Mayo**!Ndikufa kuno.
   A. Mvekero C.Mlowammalo
   B.Mperekezi D.Mfuwu
8. **Kondwani** watenga zake.
   A.Dzina C.Mlowam'malo
   B.Mneni D.Mfotokozi
9. **Iwo** amadya ngati sanadyepo.
   A.Dzina C.Mlowammalo
   B.Mfotokozi D.Mlumukizi

**Mafunso 10 mpaka 14 .Sakhani magulu amayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.**

10. Anthu ambiri amakonda **mbatata**
    A.I- ,ZI- C.Mu-, Mi
    B.Li-,Ma- D.Ka-,Ti-
11. Akuba anthyola **chitseko** changa
    A.I-, Zi- C.U-,Ma-
    B.Chi-, D.Zi-Mu-,Mi-
12. **Kambalame** kaja kafa
    A.Li-, Ma- C.Ka-,Ti-
    B.I-,Zi-, D.U-, Ma-
13. **Kalata** yamchezo ndi yosavuta kulemba.
    A.Ka-,Ti- C.Ku-,Pa-, Mu-
    B.I-,Zi-. D.Chi-, Zi-
14. **Mnyumba** mwawo mwalowa njoka.
    A.Ku-nditsindenyumba C.I-, Zi-
    B.Ku-,Pa- Mu- D.Mnyu-,mba-

**Mafunso 15 mpaka 20, Sakhani nthawi za aneni zomwe zili ndi mzere kunsi kwawo**

15. **Ankavina** bwino m'ganda alimtsikana.
    A.Yatsopanoyawamba C.Yakale yathayi
    B.Yamtsogolo D.Yakale yopitiliza
16. **Ndizidzaku** gwadila ukadzandikwatira
    A.Yakalec. C.Yamtsogoloyanthayi
    B.Yatsopanod. D.Yamtsogoloyopitilira
17. Gama **akulima** m'munda umo.
    A.Yatsopano yathayi C.Yatsopano yopitilira
    B.Yatsopano D.Yakale
18. A Phunzitsi **anandigwiritsa** chibalo
    A.Yatsopano C.Yakale yathayi
    B.Yakale D.Yamtsogolo.
19. **Ndizakhala nditafika** ukamazabwera
    A.Yamtsogolo C.Yamtsogolo yathayi
    B.YakaleyopitiliraD.Yamtsogoloyopitilira.
20. **Adakhala akuyimba** utsiku onse.
    A.Yatsogolo C.Yakaleyopitilira
    B.Yakale D.yakaleyathayiyopitilira.

**Mafunso 21 mpaka 25,Sakhani msitho wa aneni omwe watsekedwa mzere kunsi kwawo.**

21. Ndubwa **wadyetsetsa** mango
    A.Wochitirana C.Wochitira
    B.Wochititsitsa D.Wochititsa
22. Iwo **adamenywa** dzulo ndi Chopwa.
    A.Wochitiridwa C.Wonyazitsa
    B.Womenywa D.Wobwerezabwereza
23. Njinga zija **zawombana**
    A.Wochitirana C.Wotsutsa
    B.Wochititsa D.Wochitira.
24. Mwanayu wagula Malaya.
    A.Wochitira C.Womchitira
    B.Wotsutsa D.Wochitirana
25. Ndiwo zadyedwa ndi galu
    A.Wochitidwapoyera C.Wochititsitsa
    B.Wobwerezabwereza D.Wonyazitsa

**Mafunso 26 mpaka 30,Sakhani matanthauzo oyenera a mikuluwiko yotsatirayi.**

26. .ndaonera momwemu mwambi wa gulugufe
    A. Kuyenda mofulumira
    B. Kukhutira nzomwe uli nazo
    C. Kuuluka ndi mapiko
    D. Kusangalala ndi maluwa

**27.** Nyumba ya mwini saotchers mbewa
   A. Mnyumba ya mwini sitimasuka
   B. Nyumba ya mwini umadya bwino
   C. Usamadalire kwambiri zinthu za eni
   D. Usadalire kwambiri zinthu zako.

**28.** Kulamula vumbwe kulinga uli ndi nkhuku
   A. Umathamangitsa vumbwe poti uli ndi ziweto
   B. Kupalamula mulandu chifukwa cha mphamvu
   C. Munthu usamapalamure ulibe populumukira
   D. Kupalamula mulandu nkulinga uli ndi pogwira

**29.** Nkhondo ndi anansi
   A. Abale amatikonda pa mtendere pokha
   B. Abale nthawi zina amakufunira zoipa
   C. Abale nthawi zina sayamika
   D. Abale saoneka pamavuto

**30.** Suzumile adaphetsa mkhale mkale
   A. Kusaugwira mtima kumadzetsa mavuto
   B. Kusasamala kumaonongetsa zinthu
   C. Anthu okalamba amafa mwadzidzidzi
   D. Sibwino kuchita zinthu mwachangu

**Mafunso 31 mpaka 35,Sakhani mitundu ya afotokozi omwe ali ndi mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatilazi**

**31.** 32.Mnyamata **<u>wamphamvu</u>** akukakha galimoto
   A.Wamaonekedwe C..Waumwini
   B.Wamskhalidwe D.woloza

**32.** Mbewa **<u>ija</u>** yaphedwa ndi mphaka
   A. Waumwini C.Woloza
   B.Wamakhalidwe. D.Wochuluka

**33.** Aphunzitsi alowa m’kalasi **<u>mwawo</u>**
   A. Woloza C. wamaonekedwe
   B. Waumwini D.Wochuluka

**34.** Mbuzi **<u>khumi</u>** zagundidwa ndi galimoto
   A.Wowerenga C. wamaonekedwe
   B.Woloza D.Waumwini

**35.** Pepala **<u>loyera</u>** limodzi limawala bwino polembapo
   A.Woloza C. Wamaonekedwe
   B.Waumwini D.wamgwirizano

**Mafunso 36 mpaka 38,Sakhani mawu otsutsana ndi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m’ziganizo zotsatirazi**

**36.** **<u>Adam’kwizinga</u>** dzuwa likulowa
   A.Adam’menya C..Adam’masula
   B.Adam’lasa D.Adamtulutsa

**37.** **<u>Kugomo</u>** ilo kuli njoka zambiri
   A.Dera C..Phiri
   B.Manda D.Chigwa

**38.** **<u>Umphawi</u>**wafikapachimakemasikuano
   A.Umbuli C.Kalangale
   B.Kulemera D.Umbava.

**Mafunso 39 mpaka 44. Sankhani Mitundu ya mayina omwe ali ndi mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi**

**39.** **<u>Ubale</u>** ndi fupa siliola mwachangu
   A.Lopandaumwni C.Lokhuzika
   B.Lotsakhuzika D.Launyinji

**40.** **<u>Chimwemwe</u>** wakhoza mayeso.
   A.lamwinimwini C.lopandamwinimwini
   B.lachithuchotsakhuzika D.la unyinji

**41.** Abambo asenza **<u>mtolo</u>** wanzimbe
   A.lachibalec. la mwinimwini
   B.launyinji D.lopandamwinimwini

**42.** **<u>Uchikumbe</u>**umabweletsandalamam’dziko
   a.lachithuchokhuzikac la unyinji
   b.lachithuchotsakhudzikad.la mwinimwini

**43.** **<u>Msambi</u>**wankhosawalowam’mundamwathu
   a.lachithuchotsakhudzikac .la mwinimwini
   b.lopandamwinimwinid.la unyinji.

**44.** **<u>Nyani</u>**wadyachimangam’dimbalawo.
   A. lachibalec. la unyinji.
   B. lamwinimwini
   C. lopandamwinimwini
   D. la chinthuchosakhudzika.

**MAFUNSO ATHERA TSAMBA ILI.**
**GAMA G**